Zimene Mungachite Kuti Mulungu Apitirize Kukukondani (Gawo 2)

Zoti muchitezi zachokera m'mutu 19 wa buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mofatsa zimene mumakhulupirira komanso chifukwa chake mumazikhulupirira, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, komanso onani mmene mungafotokozere zimene mumakhulupirirazo kwa ena.

KODI MUNGATANI KUTI MUSASIYE KUKONDA MULUNGU?

1 GANIZIRANI MOFATSA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena anganene chiyani?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

N'chifukwa chiyani mumazikhulupirira?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Kuphunzira Baibulo patokha ndi kupemphera kumatithandiza kuti tikhale pa ubwenzi ndi Mulungu.
(Onani mutu 19 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 10-14.)

Werengani Miyambo 2:1-5; Yohane 17:3; 1 Timoteyo 4:15.
Kodi mumapindula bwanji mukamaphunzira komanso kuganizira kwambiri mfundo za m'Baibulo?

Werengani Salimo 62:8; 1 Atesalonika 5:17.
N'chifukwa chiyani tiyenera kupemphera nthawi zonse?

Khala limene lili pa makala anzake limapitirizabe kuyaka. Mofanana ndi zimenezi, Mkhristu amene amalambira Mulungu ndi Akhristu anzake amakhala pa ubwenzi wolimba ndi Mulungu

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Yehova amafuna kuti tizimulambira limodzi ndi Akhristu anzathu.

(Onani mutu 19 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 15-23.)

Werengani 2 Timoteyo 4:2; Aheberi 10:24, 25.

Kodi tiyenera kuiona motani ntchito yolalikira komanso kusonkhana ndi Akhristu anzathu?

Werengani 1 Timoteyo 6:12.

Kodi Mulungu walonjeza kuti anthu amene amamulambira ndi Akhristu anzawo adzawachitira zotani m'tsogolo?

Kodi kusonkhana limodzi ndi Akhristu anzanu **kwakuthandizani** m'njira ziti?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

Nkhani za chipembedzo ndi zachinsinsi zimene sitiyenera kukambirana ndi anthu ena.

MUNGANENE KUTI…

Anthu ambiri akhoza kugwirizana ndi maganizo amenewo. Koma ndimakhulupirira kuti Akhristu ayenera kuuza ena zimene amakhulupirira chifukwa…

_____

_____

Kodi ndi lemba liti limene mungamuwerengere munthuyo?

_____

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungalifotokoze bwanji lembalo?

_____

WINA AKANENA KUTI…

Tiyenera kuchita zili zonse zimene tingafune panopa chifukwa moyo ndi wokhawu umene tili nawo.

MUNGANENE KUTI…

Ndi zoona kuti sitiyenera kuona moyo mopepuka. Koma ndimakhulupirira kuti moyo si wokhawu chifukwa…

_____

_____

Kodi ndi lemba liti limene mungamuwerengere munthuyo?

_____

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungalifotokoze bwanji lembalo?

_____

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania